

KULINDIRA

CHIYEMBEKEZO CHODALA



Ndi maonekedwe a ulemelero a ulemelero wa Mulungu wankulu ndi mpulumutsi wathu Yesu Khristu (Tito 2:13).

Anthu timaphweketsa zinthu zitatatu zofunikira kwambiri kuti tikhale ndi moyo monga: mpweya, madzi ndi chakudya.

Munthu amafa ngati akhala mphindi zochepa popanda mphweya ndi masiku achepa popanda madzi komanso mwezi umodzi popanda chakudya.

Popanda chikondi timafa. Izi zimaonekera mwa anthu okuda amnzawo ndi a nkhwizi osakhululuka, ankhansa ndi opanda chifundo. Ambiri mwa iwo amakhala otafa mkati mwao kuti tikhale ndi moyo tikunikanso chikhulupiliro ndi chiyembekezo. Ziwirizi zimayenda limodzi koma chiyembekezo ndi chofunikira kwambiri.

Mulungu anakonzika kuti tidzikhala ndi chiyembekezo, ndipo popanda icho, timafa. Munthu akafika potaya chiyembekezo, nalo thupi lake limaonetsa ndipo limayamba kufa. Ngati munthu wataya chiyembekezo, chifukwa chokhalira ndi moyo ndikulora kukhumudwa kutenga ulamuliro pa moyo wake, zimabweletsa mavuto ambiri ngakhale kufuna kudzipha.

Zosautsa za dziko lino zitha kuononga chiyembekezo cha munthu, komabe chiyembekezo chochokera kwa

Mulungu ndi Nangula wa moyo wathu ndipo sichizatilepheletsika. *“Chimene tilinacho ngati nangula wa moyo chokhazikika ndi cholimbanso, ndi chakulowa nkatikati mwa chopimba”.*

Ngalawa yomwe yakhazikika, imalimba pa namondwe alyense, ndiye munthu amenenso waimikika mchiyembekezo cha Mulungu amapilira mmasautso onse adziko lino.

Kodi chiyembekezo ndi chiyani? Chiyembekezo ndi chidaliro, ngakhale chikhumbo chofuna kulandira, kudikilira ndi chidaliro, kukhazikitsa chokhumba chathu pa munthu yemwe chiyembekezo chathu chili.

Chiyembekezo chathu nchokhazikika pa munthu wotchedwa Yesu Khristu amene akubwera chifukwa cha ife monga momwe buku lopatulika linalankhulira ndi kulonjeza. Anabwera koyamba molingana ndi mmene Buku lopatulika linalonjezera, ndipo adzabweranso molingana ndi mmene likulonjezera.

Buku lopatulika limationetsa umo mmene Yesu Khristu adzabwere kudzatenga okhulupilira ache. Adzatsika kuchoka kumwamba ndi mfumu ndi kulira kwa lipenga lalikulu. Choyamba okufa mwa Ambuye adzaukitsidwa ndi matupi atsopano ndi kukumana ndi Khristu mlengalenga. Ndipo kenako amoyo adzandira matupi aulemerero ndipo udzakumana ndi Khristu mlengalenga ndipo thupi la ulemelero limeneri silizagwidwanso matenda kapena chivundi koma lizakhala ndi Mulungu kwa muyaya. Izi zizachitika mofulumira kwambiri mkaphindi ndipo Yesu azatitengera kumwamba.

Afilipi 3:21 Amene azasanduliza thupi lathu lopepulidwa, lifanane nalo thupi lache la ulemelero.

Kukumana kwa Yesu ndi okhulupilira ake mlengalenga ndikuwatengera kumwamba ndicho chiyembekezo chodala. Ichi ndicho chiyembekezo chimene okhulupilira amakhala ndi moyo chimene

sichingachotsedwe kapena kuonongedwa. Ndi nangula wa moyo wathu.

1 Atesalonika 4:16,17. Pakuti Ambuye adzatsika kumwamba mwini yekha ndi nfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka. Pemenepe ife okhala ndi moyo osalafe tidzakwatulidwa nawo pamodzi mmitambo kukakumana ndi Ambuye Mlengalenga ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.

Ndipo Yesu Khristu atakumana ndi okhulupilira mlengalenga, chotsalira adzatitengera azatitengera kumwamba kumene ndi maso athu tidzaona Mulungu atakhala pa mpando wache wachifumu ndi ulemelero wache wonse. Baibulo limalongosola za Mulungu pa mpando wache wachifumu wokhala ndi kuwala kwa mitundumitundu yosiyanasiyana yokongola kumene kuli mphezi ndi kung'anima mophatikizana ndi nyali yoyaka moto.

Chifukwa chakuti Yesu Khristu ndiye chiyembekezo chathu chodala, sitizaopa. Pansi pa mpando wachifumu wa Mulungu pali Nyanja ya mandala ndipo ndipo okhulupilira adzaima pa Nyanja ya mandala imeneyi.

Ataima pamaso pa Mulungu Atate, okhulupilira ndipo adzatengeredwa kumene Baibulo limanena kuti ku phwando lamwana wankhosa Udzakhala mwambo wodabwitsa kwambiri. Udzakhala ngati mwambo waukwati womwe ukhalira padziko lapansi pomwe abwenzi ndi apabanja onse amakumana kusangalala ndi nyimbo ndi zakudya zamitundu yonse. Kumakhala kuvina ndi kukumana ndi abwenzi ndi abale omwe timawakonda komanso omwe tinawasowa. Mkwatibwiyo amakhala atabala chovala cha ukwati chokongola ndi choyera ndipo kumwamba, ife okhulupilira tidzakhala titavala zoyera monyezimira. Pali kulumikizana pakati pa Mulungu ndi anthu ake.

Chibvumbulitso 19:8,9 Ndipo anampatsa iye abvale bafuta wonyezimira woti mbu;pakuti bafuta ndiye zolungama za oyera mtima.Ndipo ananena ndi ine, Lemba Odala iwo amene amene aitanidwa ku phwando la mwana wankhosa.Ndipo ananena ndi ine,Iwo ndiwo amawona Mulungu.Buku lopatulika ndipo litiwonetsa kumudzi kwathu kumamba kumene kumatchedwa Yerusalemu watsopano ndiwoyera.Mzinda umenewu ndiwaukulu kwambiri mawonekedwe ake.Umaoneka monga dziko lachikhalire.Maziko ake ndi amiyala ya mtengo wapatali amene adzawale ndi ulemelero wa Mulungu. Mzinda wodzala ndi miyala ya mtengo wapatali ya golide ndi krustalo, zomwe zipangitsa kuoneka ngati mwala owala ndi ulemelero wa Mulungu;

Chibvumbulitso 2:10,11¹⁰- Ndipo ananditenga mu Mzimu kunka ku phiri lalikuru ndi laltali, nandionetsa mzinda wopatulikawo,Yerusalemu,wotsika m'mwamba kuchokera kw Mulungu,¹¹ndipo unakhala nawo ulemelero wa Mulungu;kuunika kwacha kunafanana ndi mwala wa mtengo wache woposa,Ngati wayaspi,wonyezimira,ngati krustalo.

TINGAPEZE BWANJICHYEMBEKEZO CHODALA NDI KUKHALA NDI MULUNGU KWA MUYAYA?

Yohane 3:16 Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koteru kuti anapatsa mwana wache wobadwa yekha,ku yense wokhulupilira iye asataike,koma akhale nawo moyo wosatha.

Musanafike pokhala ndi chiyembekezo chodala ndikukhala ndi moyo wosatha,dipo la uchimo liyenera kuthetsedwa.Mulungu ndi Woyera ndipo tchimo lamunthu ndi mlandu waukulu.Chilango chache ndikulekana kosatha ndi Mulungu kumalo oopya otchedwa gehena.

Pamene Yesu kristu anafa pamtanda, ndikukhetsa mwazi wake ,analipira dipo la uchimo wathu.Ndiye

chifukwa cha dipo analipira Yesu,tsopano muli nd chitsimikizo chonse cha moyo wosatha ndi Mulungu.Ysanangofa kokha chifukwa cha machismo anu,komanso anaukwa akufa ndi thupi la ulemelero. Choncho mukhoza kukhala ndi chiyembekezo chodala! Mulungu amakukondani koma kuti mukhale ndi chiyembekezo chodala chimenechi,muyenera kulapa machismo anu ndi kubvomeleza Yesu kristu kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanu.

Aroma 6:23 Pakuti mphoto yache ya uchimo ndi imfa;koma mphoto ya ulele ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Amuye wathu.

PEMPHERO LOMULANDIRA YESU KRISTU NDIKUKHALA NDI CHYEMBEKEZO CHODALA.

Ambuye ndikubvomeleza tchimo langa kwa inu ndipo ndikulilapa. Ndikukhulupilira kuti Yesu anakhetsa mwazi wache pamtanda ndikufera machismo anga. Ndikhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo adzabwelanso. Tsopano ndikubvomeleza Yesu kristu ngati mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanga.Tsopanoi ndili ndi moyo wosatha ndi inu monga Tate wanga ndipo ndi ndi chiyembekezo chodala.

Ndikupemphani Tate Mulungu wanga kuti muchilitse mtima wanga wosweka.Ndakhululukira onse anasw mtima wanga.Chonde Atate, chilitsani ndikundimasula ku mantha,nkhawa zoopsa,udani,kukhumudwa,kuipa mtima ndikukanidwa.

Zikomo kwambiri chifukw chotumiza Yesu kristu kudzandimasulaku uchimo ndikuchulitsa mtima wanga wosweka.



Scan for teaching testimonies and radio archives on the brokenhearted ministry or visit bind.brokenhearted.com

Chaplain John P Mc Ternan, Ph.D

USA Prophecy.com

MC T011@AOL. Com